


MUOMBOLI WANGA ALIMOYO

 Moni wa Isitara kwa inu nonse, mmawa uno. Wokondwa kwambiri kuti ndiri pano, lero, mu kachisi, pa nthawi ya chikumbutso chachikulu ichi cha Isitara. Ambuye atipatsa ife tsiku lokongola la kupembedza uku. Ndipo ife tiri pano mmawa uno mu chikondwerero cha chochitika chachikulu chimene chinayamba chachitikapo mu dziko, chiwukitsiro cha Ambuye wathu Yesu. Iye anali wamkulu mu imfa Yake, koma anthu akhoza kufa, koma sipanayambe pakhala munthu yemwe anakhoza kuwuka kwa akufa koma Iye. Ndipo apo ndi pamene ziyembekezero zathu zagona mmawa uno, mu chiwukitsiro cha Ambuye wathu.

² Pamene ine ndinali kubwera muno, mmawa uno, ndikuyenda kudutsa mu kampita, ine ndinaima mphindi zingapo kumbuyo uko kuti ndiyang'ane. Ndinayang'ana mozungulira pa omvetsera, ndipo ine ndinaganiza, “Kutuluka molawirira, mmawa uno, anthuwa anali, pansu pa ziyembekezo, kuti abwere kuno ndi kudzamva Mawu ali kuwengeredwa, ndi nyimbo zikuyimbidwa. Ndipo ndi chikumbutso cha Mmodzi Yemwe akugwirizira miyoyo yathu mu dzanja Lake lero.” Ine ndinaganiza za nkhope zimene ine ndinkaziwona molawirira mmawa, zaka zapitazo. Izo zagona mu manda awa kuzungulira kuno, zikuyembekezera kuchitika kwa chiwukitsiro chawo.

³ Kuganiza za izo, bwanji, izo zikutibweretsa ife ku ganizo ili, kuti, lero ife tiri pano. Ife sitiri kudziwa basi nthawi imene ife titi tidzatengedwere ku malo a—a kumene iwo agona mmawa uno. Ndiyeno, izo ziri powonekera, ndi anthu a mtundu wanji omwe ife tiyenera kukhala, ndi momwe ife tiyenera kuyandikira pa chiwukitsiro ichi cha lero?

⁴ Mu Bukhu la—la Yobu, mu wa 10 . . . mutu wa 19 ndi ndime 25, Mawu pang'ono awa.

. . . *ine ndikudziwa . . . muomboli wanga alimoyo, . . .*

⁵ Unali uneneri wa Yobu ndi mawu ake, iye atawona kaye tsiku lino limene ife tiri kupembedza lero, kupembedzamo, chiwukitsiro.

⁶ Ine, powoloka kuzungulira ku mbali za mdziko, ndi kuwona mawonekedwe osiyana a chipembedzo, ndi magawo osiyana a kupembedza, izo zikanati zitenge nthawi motalikirapo, kuti tipitepo, kuti tiyesere kufotokoza zopambana zosiyana za chipembedzo cha mdziko ili.

⁷ Koma, lero, pozindikira kuti ife tiri nalo patsogolo pathu tsiku lalikulu, ndipo kuti ife tasonkhana pano, mmawa uno, basi ku kupembedza uku kwa molawirira mmawa uno kwa

mphindi pang'ono. Ife tibwerera ndiye ku manyumba kwathu, ndi kukabwerera ku, chimene ife tikuchidalira lero, msonkhano wamachiritso.

⁸ Ife sitinakhale nawo konse iwo koma kawiri kapena nthawi zitatu, chiyambireni ife tiri—takhala pa . . . mu misonkhano. Chifukwa, kawirikawiri, kubwera ku kachisi ndi kozungulira, anthu akwathu kuno, kudzoza kwa Mzimu Woyera kumawoneka ngati Iko sikumabwera bwino basi, pano, chifukwa ndi kwathu. Kamodzi izo zinachitikapo, ndi uko ku Jeffersonville High School; ndiyeno izo zinachitikapo kamodzi kuno ku kachisi.

⁹ Ndipo kochokera pamene ine ndinawuka mmawa uno . . . ine mwakuwoneka ndabwera muno mochedwerapo pang'ono, koma izo zinali pa cholinga. Ine ndinali nditawuka mmawa uno, kale tsiku lisanayambe, ndipo ndimadikira.

¹⁰ Ndipo ine ndikungokhulupirira kuti ife tikupenyana ndi utumiki waukulu lero, mu utumiki wa machiritso. Ndipo anyamata, ife tiwapatsa iwo makadi tsopano, ndipo iwo awapereka iwo mmawa uno mma 9 koloko, a mautumiki amachiritso amene akudzapo. Ine ndikukhulupirira Ambuye atipatsa ife nthawi yaikulu.

¹¹ Chotero, ife timupembedza Iye mu pemphero ndi mu nyimbo, ndi kuyankhula kwa Mawu, ndiyeno tiyesera kuti tichokeko lero, mmawa uno, mma seveni, ngati nkotheka, chotero munthu aliyense akhoze kukabwerera ndi kukhala nayo nthawi yokwanira kuti apange kukonzekera kwa utumiki.

¹² Makadi a pemphero adzakhala akuperekedwa pa naini pomwe, chotero kuti izo zisati zisokonezane ndi mautumiki ena onsewa.

¹³ Ndiye, usikuuno, ndithudi, pakhala mautumiki a ubatizo, naponso. Ife tikukhumba kuti inu nonse mudzakhalepo pa izi, alendo mu zipata zathu, ndi ena otero. Ife tiri okondwa kwambiri kukhala nanu inu pano mmawa uno, kudzawona utumiki wa kutuluka kwa dzuwa uwu, ndi kachisi wodzaza.

¹⁴ Tsopano, pa malingaliro osiyana tsopano, lero, a kupembedza kwa chipembedzo. Mu malo ambiri, iwo akupembedza amakezana amene anapita kale. Mwa chitsanzo, ngati ife titati tipite ku China mmawa uno, ndi kukayankhula Mawu okuti Mulungu, kapena ku Japan, iwo akanati adabwe mulungu yemwe iwe unali kumukamba, chifukwa, munthu aliyense amene amafa, ndi mulungu mwamsanga pamene iye afa. Ndipo ngati ife titati tipite kumene opembedza Buddha ali, kapena osiyana, Achimuhamadi, iwo samakhulupirira kuti Khristu anawuka kwa akufa. Iwo samakhulupirira kuti iye anafa nkomwe. Iwo amati, “Iye anakwera pa kavalo ndipo anakwera nachoka anapita Kumwamba.”

¹⁵ Koma, lero, ife tiri nacho kwenikweni Choonadi ndi Kuwala kwa Moyu. Palibe kukaikira mu malingaliro anga,

lero, monga—mlaliki wa Uthenga wa Chikhristu. Ine ndiribe kukaikira nkomwe mu malingaliro anga, palibe mthunzi umodzi wa kukaika, koma kuti ife motsimikiza tiri nacho Choonadi chosindikizidwa. Kuti zipembedzo zina zikhoza kukhala zolondola, koma ife tiri nacho Choonadi.

¹⁶ Ngati ife tikuzindikira, lero, izo, popenya nyengo. Ndithudi Mulungu wamkulu wa Kumwamba, Yemwe anapanga miyamba yonse ndi dziko lapansi, anapanga... Ngati inu mungakhoze kuwona momwe malingaliro Ake anali kuyendera, momwe Iye aliri nako kugwa masamba kwa mchaka, imfa; ndiye kuphukira kwa mchaka, chiwukitsiro. Polinga kuti, iwe umayenera kuti ufe, polinga kuti ukhale ndi chiwukitsiro.

¹⁷ Ndi kupyolera mu imfa yomwe nthawizonse imabweretsa moyo. Iwe umakhala moyo kokha kupyolera mu imfa. Kodi inu munayamba mwaima kuti mulingalire zimenezo, kuti mtundu wa anthu umakhala moyo kupyolera mu imfa? Chinachake chiyenera kuti chife kuti iwe ukhoze kukhala moyo; chakudya. Moyo wa zomera, moyo wa zinyama, zonse zimafa. Ndipo kupyolera mu imfa imeneyo, ife timadya chakudya. Ndipo chakudya chimene ife timadya, zinthu zakufa za chinachake, zimabala makhungu a moyo wa magari umene umabwera mu thupi lathu. Chotero ife timakhala kokha moyo, ndi kumakula, ndi kumapuma, ndi kumadya, ndi moyo, ndipo tsopano... ndi mwa imfa. Ndipo ife tiyenera kukhala ndi imfa polinga kuti tibale moyo, ndiye.

¹⁸ Tsopano, uthenga uwu umene unawerengedwa kwa ife, mmawa uno, ife tikanati tiwutche iwo kutuma kwakukulu, pakuti iko kunali kutuma kotsiriza kumene Ambuye wathu anawapatsa ophunzira Ake. “Kuti apite ku dziko lonse, ndi kuti akalalikire uthenga waulemerero uwu, nkhani yabwino ya chiwukitsiro, kwa dziko lonse, mwa umboni.” Ndiyeno Iye akanati abwerere. “Ndi kuti zizindikiro ndi zodabwitsa zikanati zitsatire Uthenga uwu umene unali woti uzilalikiidwa.”

¹⁹ Ndipo lero, mu maiko, ife timapeza ngakhale pansu pa chipembedzo cha Chikhristu, kuti ife timapeza anthu mu Amereka, ambiri a iwo, ali ndi kulemekeza konse kwabwino ndi koyenera kwa izo, ife tiri kuyesera kuti tipeze mipingo yaikulu, ndi makachisi, ndi madongosolo aakulu, ndi zina zotero, naponso. Pa Isitara, lero, mipingo yaikulu ndi mitanda ziri kupukutidwira ku utumiki wawukulu uwu wa Isitara. Ndipo, lero, kwenikweni makumi a zikwi ndi mamilioni a madola zikhala zitaonongedwa chifukwa cha maluwa a Isitara ndi zina zotero, kuti zipite pa maguwa, kuti akongoletse matchalitchi aakulu awa ndi makafiduro amene ife tiri nawo lero.

²⁰ Ndipo mu Roma, likulu la mpingo wa Katolika, mmenemo iwo... mosungira mitembo mwamukulu muja, mwa Petro Woyera, kumene anthu akufa anaikidwamo. Iwo amakonda

kunena, mu mpingo wa Katolika, kuti, “Ife tiri nacho icho, chifukwa ife tiri nalo thupi kuno la Petro Woyera, lagona muno. Ife tiri nalo thupi la atumwi osiyana, ndi ophunzira, ndi amuna aakulu amene anafa ndipo ali. . . Matupi awo anaikidwa muno.” Ndipo iwo amayang’ana pa chimenecho ngati kuti icho chinali kutsimikizira kwina kwakukulu ku gawo lawo la chipembedzo, kuti iwo ali naye Mulungu.

²¹ Koma icho nthawizonse chakhala chotsutsa changa, abwenzi, kuti zinthu zimenezo sizimatanthauza kanthu. Izo sindizo. Munthu aliyense akhoza kufa ndi kugona mu nthaka. Koma Chimene chinawuka kuchokera mmenemo ndi chimene ife tikuchipembedza lero, Ambuye Yesu wamoyo, wowukitsidwa, wokwera mmwamba Amene akukhala moyo lero. Anthu ambiri akhoza kufa.

²² Lachisanu latha, anthu anakwawa pa maondo awo, kukwera masitepe aku Vatikani. Ndipo anthu ambiri anakalowa umo ndipo anakakondwerera imfa, imene inali. . . chinthu chachikulu ndi changozi chimene chinachitika kwa Khristu. Koma Iye anayenera kuchita zimenezo polinga kuti atsimikizire kuti Iye anali Khristu.

²³ Koma lero ndi tsiku, chiwukitsiro, ichi chinasindikiza izo kwa nthawizonse. Tsopano Iye sali wakufa. Iye ali wamoyo, lero, akukhala moyo mu mtima uliwonse ndi munthu aliyense.

²⁴ Amuna akale, pamene iwo anali kuyang’ana mtsogolo ku tsiku lino, m’badwa zakale mmbuyo mu Baibulo; Abrahamu, Isaki, Yakobo, Yobu. Ochuluka a mbadwa zakale ankayang’ana mtsogolo ku nthawi yomwe Khristu akanati adzawuke kwa akufa.

²⁵ Ine ndikuganiza za Yobu, mmodzi yemwe ife tinali kumuwerenga mphindi pang’ono zapitazo, ankayang’ana mtsogolo ku mmawa uwu. Pamene iye anali wokalamba, wokanthidwa mu usinkhu, ndipo mnofu wake unali mophweka ukugwa kuchokera pa thupi lake, ndi zirona. Mtima wake unali utasweka, mwa chisoni. Ndipo gawo lirilonse la chivundi la umunthu wake linali likunyalapo.

²⁶ Ndipo munthu wamkulu monga uyo, yemwe anapanga chokopa chachikulu kwa dziko mu tsiku lake; ndipo powona kuti, zonse zimene iye anali—iye anali, ndi kukula. Iye anati iye amakhoza kupita ku mizinda ya Kummawa, ndipo akalonga amakhoza kugwada pamaso pa iye, pa kulingalira za nzeru zake.

²⁷ Koma pano iye anali, pa mapeto a nyonga zake. Chirichonse chinali chitapita, mwakuwoneka. Thupi lake linali litapita. Chuma chake chinali chitapita. Ana ake anali atatha. Zonse zimene iye anali nazo zinali zitapita.

²⁸ Ndipo, ndiye, Mulungu mu chifundo Chake anabwera pansu kwa Yobu, ndipo Iye anamupatsa iye mphamvu ina, kuti iye akhoze kutsegula maso ake ndi kuliwona tsiku limene pakanati

padzakhale thupi limene iye akanati adzalilandire. Iye anadziwa kuti panali kubwera Mmodzi, Mmodzi Wolungama, Yemwe akanati adzaimu mu malo ake, Yemwe akanati adzawukitse thupi la akufa, ndipo akanadzatero. Iye anati, “Ine ndikudziwa kuti Muomboli wanga alimoyo.” Ine ndimawakonda mawu otsimikiza awo amene iye anayankhula mu izo.

²⁹ Osati, “Ine ndikuyembekeza chomwecho. Ine ndiri nako kumverera kuti kudzakhala kuli.” Ndicho pafupi katengedwe ka ochuluka lero, “Ine ndiri ndi chiyembekezo kuti tsiku lina . . .”

³⁰ Koma Yobu anali nacho choposa icho. Iye anati, “Ine ndikudziwa Muomboli wanga alimoyo,” mbali yotsimikiza ya izo. Osatinso mu kukaikira. Izo zonse ndi zotsimikizika.

³¹ Ndipo ngati lero, ngati ife tikanangokhala ndi mtanda pamwamba pa tchalitchi, kuti tisonyeze chimene . . . Izo ndi zabwino, kuti Khristu . . . Iye timakhulupirira mu imfa ya Khristu, kuikidwa, ndi chiwukitsiro. Ngati ife tikanangokhala ndi matupi afumbi angapo akufa atagona pansu pa mpingo, ndi ena a anthu oyerata ikidwa mkatimo, amene kuti . . . Iye tikanangokhala nazo izo ngati chiyembekezo, ndiye ife tiri pakati pa anthu onse omvetsa chisoni kwambiri.

³² Koma, lero, ndife oyamikira bwanji! Iye tiribe matupi akufa, koma ife tiri nawo Mzimu wowukitsidwa wa Ambuye Yesu Khristu, kuti Iye anawuka kwa akufa, mwachigonjetso.

³³ Izo siziri panonso, “Ine ndikulingalira chomwecho.” Iwe ukhoza kuyang’ana pa mtanda ndi “kulingalira chomwecho.” Iwe ukhoza kuyang’ana pa thupi litagona mu nthaka, ndi kuti, “Ine ndikulingalira chomwecho,” ndipo “Ine ndikuyembekeza chomwecho.”

³⁴ Koma pamene masomphenya amene anamugunda Yobu ayamba atakhala chenicheni, chiwukitsiro cha Ambuye Yesu mwa Mzimu Woyera mu mtima, ndiye iwe uli ndi, “Ine ndikudziwa Muomboli wanga alimoyo.”

³⁵ Mithunzi yonse yazimirira, mdima wonse wakale wa, “ndikuyembekeza chomwecho,” ndi “mwina chomwecho,” ndi, “ife tikudalira izo zikhala mwanjira imeneyo.” Izo zonse zazimirira kutali, kwa aliyense yemwe anayamba wapanga mtima wake manda kwa Ambuye Yesu Khristu.

³⁶ Anafa ndi Iye, anaikidwa ndi Iye, ndipo anawuka ndi Iye! Anawuka ndi Khristu mu chiwukitsiro! Chiyembekezo chatsopano ichi chimene Mulungu wachikhazikitsa mu mitima yathu, lero, chitsimikizo chatsopano ichi! Ndi chiyembekezo kwa iwo amene akuyang’anira mtsogolo ku nthawiyo. Koma pamene mwamuna kapena mkazi wakhala atawukitsidwapo katsopano, ndizo “ndikudziwa chomwecho” tsopano. “Ine ndikudziwa Muomboli wanga alimoyo. Chifukwa? Iye ali moyo mkati mwa mtima wanga.”

37 Kodi sindicho chododometsa lero kuti mithunzi yonse yadutsa kale? Zonse. . . “Chabwino, ine ndikuyembekeza kuti ine ndidzabwera mu chiwukitsiro.” Palibenso “chiyembekezo.” Ife tiri nacho chitsimikizo! Ndizo zonse. Ife tikudziwa izo. Palibenso “kuyembekeza chomwecho.”

38 Chifukwa, chinachake chachitika mu miyoyo yathu, chimene chatengera mithunzi yonse kutali, pamene Khristu Mmodzi wowukitsidwayo anabwera ku zikhaliidwe zathu zochimwa zimene ife tinalimo. Ndipo zinthu zakale zinafa, mu kupachikidwa ndi Iye, pa guwa. Ndipo ife tinawuka mwatsopano, kachiwiri ndi Iye, ndipo tikukhala moyo ndi Iye ndi kulamulira ndi Iye. “Ndipo takhala tsopano mu malo a Mmwambamwamba mwa Khristu Yesu.” Ife tawukitsidwa kale ndi Iye. Chiwukitsiro chadutsa kale, monga momwe ife tikukhudzidwira, chifukwa ife tiri tsopano owukitsidwa ndi Khristu. Amen. “Tikukhala mu malo a Mmwambamwamba mwa Khristu Yesu.”

39 Palibenso “kulingalira” za izo. Izo zonse zatha. Amen. Ine ndikungozikonda izo. Palibenso “ziyembekezo,” palibenso “kukhumba,” palibenso. O, izo zatha.

“Ifi tiri tsopano owukitsidwa ndi Iye, tikukhala mu malo a Mmwambamwamba.”

40 Ndipo tsopano, ndipo mkati ndi pamwamba pa izi, kwa Mpingo! Inu mukuti, ndiye, “M’bale Branham, kodi izo zikutanthauza chiani, ndiye, kuti ife tiyenera ‘kumalalikira Uthenga’ wake?” Ndicho chiyembekezo chathu chotsatira. Ndicho chinthu chathu chotsatira. Ife titawuka kale ndi Iye, ife tiri nako kutumidwa kwakukulu, kuti tipite mu dziko lonse ndi kukabweretsa nkhani zabwino izi kwa ena.

41 Ndi mmawa wokongola bwanji, pamene Maria wa Magdalena, Maria amake, anabwera kumanda molawirira mmawa uja, akudabwa, “Ndani ati akatigudubuzire chimwala pa manda? Ndani ati akakhoze kukachotsapo chimwalacho?” Iwo anapitirira, patsogolo, mwa chikhulupiriro, akukhulupirira. Ndipo pamene mmawa unayamba kutulukira, aphwiti ndi zonse zinasiya kuyimba kwawo. Ndipo chinthu choyamba, nyenyezi ya mmawa inayatsa njira, ndipo ngati chimwala chachikulu inayandama kudutsa pa dziko lapansi ndipo inadzapachikika pa manda pamene Iye analipo. Ndipo Mngelo anaima pamene, ndipo anagudubuza chimwalacho kuchichotsapo.

42 Ndipo Iye anawuka kuchokera mmanda, atapambana pa imfa, gehena, ndi manda. Ndipo anati, “Taonani, Ine ndiri ndi inu nthawizonse, ngakhale mpaka ku malekezero a dziko.”

43 Ndipo lero Iye ali moyo mwaukulu mu miyoyo yathu, ndipo palibenso kupeka za izo. Ine ndikuganiza Isitara ndi imodzi ya nthawi zazikulu. Ngati inayamba yakhalapo nthawi imene a Uthenga wathunthu, achipentekoste, obadwa kachiwiri, anthu

osinthika, ayenera kuti azifuula matamando kwa Mulungu, ndipo pa mmawa wa Isitara, pamene iwo akudziwa kuti icho ndi chikumbutso cha chimene chinachitika kwa iwo. “Poyamba akufa, mu tchimo ndi kulakwa; tsopano owukitsidwa, atakhala mwa Khristu, mu malo a Mmwambamwamba, tikudziwa Muomboli wanga alimoyo.”

⁴⁴ Davide, mneneri wakale, anati, “Mwakuti, thupi langa lidzapuma mu chiyembekezo, chifukwa Iye sadzalola Mmodzi woyera Wake kuti awone chivundi, ngakhale kuti Iye asiye moyo Wake mu gehena.” Kuyankhula za chiwukitsiro, kuti Mulungu akanati adzamuwukitse Khristu molingana ndi Malemba.

⁴⁵ Ndipo ife, titawukitsidwa ndi Iye lero, tiri okhazikika mwapamalo ndi Iye; ndipo tsopano takonzekera Mkwatulo kuti udze, tikuyembekezera nthawi yaikulu imeneyo. “Thupi lathu lidzapuma mu chiyembekezo.” Ife tikudziwa izo. Palibe kukaikira mu malingaliro anga lero. Palibe pang’ono pa kukaikira mu malingaliro a munthu aliyense muno, amene anayamba wabadwa kachiwiri, koma chimene iwo ati adzakhale kumeneko motsimikiza basi monga kulipo Kumwamba mmwambamo. Iwe uyenera kuti ukhale uli. Lonjezo lililonse ndi lolondola pa izo. Ndizo zonse. Ingowukitsidwani ndi Iye; ndiyeno inu mudzakhala moyo ndi Iye, mukondeni Iye, mutakhala limodzi mu malo a Mmwambamwamba, kuyembekezera nthawi yaikulu imeneyo.

⁴⁶ Tsopano, kutumidwa kwakukulu kunali, kuti apite umo. . . Iye atawuka kale kwa akufa, ndiye Iye. . . Kutuma kwakukulu kunali, koti, “Pitani mu dziko lonse, ndipo mukalalikire Uthenga kwa cholengedwa chirichonse.” Cholengedwa chirichonse chinali choti chikamve Uthenga. Ndiko kutumidwa, mmawa uno, kwa Mpingo, kuti cholengedwa chirichonse chimve Uthenga. Ndiye, pamene cholengedwa chirichonse chamva Uthenga, ndiye Yesu adzabwerera kachiwiri.

⁴⁷ Kodi inu munayamba mwaima kuti mulingalire, mmawa uno, tikanena za kubwerera, izo ziri, izo zinakhala zowoneka? Iye ali kale pano ndi ife tsopano. Iye. . . ife tsiku lina. . . Tsopano lero, tangolingalirani kuti Kukhalapo Kwake kukhala kuli pano lero. Ambuye Yesu ali mu dziko lina, kapena daimenshoni yina, pomwe pano lero mu mawonekedwe a Mzimu. Mzimu wake ukulumikizana mkati ndi mzimu wathu. Maso athu sangakhoze kumuwona Iye, chifukwa kuti iwo akadali achithupi panobe, kupatula pakanakhala chinachake chitachitika kuti ife tikanakhoza kuwona masomphenya. Koma Iye ali pano mowoneka basi, weniweni basi monga Iye anali tsiku limene Iye anayankhula kwa Maria, kumanda, kapena Iye atakomana ndi Kleopa pa ulendo wake waku Emau. Kukhalapo Kwake kuli pano.

48 Iko kukhoza kumverereka ndi zimenezo, kumvereredwa ndi mphanvu yamkati imeneyo yomwe ili mkati mwa thupi la umunthu, yotchedwa Kubadwa kwatsopano. Moyo wapatsidwa maginito a kwa Iye. Ndipo kamodzi mu kanthawi, pamene inu mulola malingaliro anu kuti akhazikike pa Iye, kukhulupirira pa Iye; pakapita kanthawi, Chinachake, chenicheni, iwe ukhoza kumverera Chinachake chikusesa pa thunthu lako. Ndicho chitsimikiziro cha chiwukitsiro Chake.

Izo si “ndikulingalira chomwecho.” Izo si “ine ndikuyembekeza chomwecho.”

49 Koma, kwa munthu aliyense yemwe ali wobadwa kachiwiri, izo ndi “ndikudziwa chomwecho.” Ndi, iwe ukudziwa izo. Izo ziri apo pomwe, ndipo pamene iwe ukhala utakhudzana ndi Iye. Ine ndawaonapo oyera akuti, “O, mungakhoze inu. . .” Kukhalapo kwa Ambuye kuli pafupi. Iwo amati, “Bwanji, pali Chinachake!” Bwanji, ndithudi. Iye ali apo pomwe. Pomwepo. . . Iye wawuka kwa akufa, ndipo Iye waima pambali panu pomwe.

50 Tsopano, tsiku lina, pamene ife tidzapita kuti tikakhale ndi Iye; mizimu iyi mkati muno, imene ingakhoze kumverera Mzimu umenewo, ukukanikizira mu Chimenecho. Ndiye, pa chiwukitsiro, pamene Iye adzadzipanga yekha kuwonekera, ife tidzapangidwa kuwonekera ndipo tidzakhala nalo thupi longa thupi Lake Lomwe laulemerero. Pakuti, pamene ife tidzabwera kuchokera ku mzimu wa chidziko, Iye adzatibweretsa ife ndi Iye. “Onse amene ali akufa mwa Khristu Mulungu adzawabweretsa ndi Iye mu chiwukitsiro.” O, ndi kuwalitsira kotani! Ndi chinthu chodala bwanji!

51 O, ngati ine ndikanati ndisatenge izi. . . O, ngati ine ndikanati ndipangidwe mfumu ya pa dziko lonse, ndi kutsimikiziridwa kuti ndikhala moyo zaka milioni; ine sindikanatenga kupembedza kwa pa chaka kwa Ambuye, ndi zinthu zimene ine ndaziwona mu chaka chapitachi, ndi kuphunzitsidwa ndi Mulungu, kwa chuma chonse cha mdziko. Chiyembekezo chodala ichi! Zitatha zaka milioni imodzi zimenezo, kapena chirichonse chimene chikanati chikhale, ine ndikanati ndileke kukhalapo.

52 Nthawizina zapitazo, M’bale Cox (wayima kumbuyo kwa nyumbayi tsopano) ndi ine tinali titakhala pa. . . Njira yoyendetsera pobwera mu nyumba, ndipo miyala ina yoswedwa inali pa msewu. Mmenemo munali chiwalo chokumbidwa chaching’ono cha nyama ina ya kunyanja, kapena chinachake, chimene chinakhala moyo zaka, zambirimбири zapitazo. Ine ndinati, “Tayang’anani pa chinthu ichi pano.”

53 Ndipo M’bale Cox anati, “M’bale Branham, ndikudabwa kuti ukale wake chomwe kwenikweni icho chiri?”

54 Ine ndinati, “Chabwino, M’bale Cox, izo mwina, owerengera zaka akanati, kupita mpaka ku mamilioni a zaka; mmbuyo

kutali dziko lapansi lino lisanayambe lakhaliidwamo ndi anthu, ndipo madzi ali ataphimba dziko lapansi. Nyama zimenezo mwinamwake zinakhala moyo zaka, zambirimbi, mamiloni ambiri apitawo. Koma ine . . .”

55 Iye anati, “Taonani, M’bale Branham,” anati, “kodi moyo waumunthu suli waufupi kwambiri, kwa moyo umenewo? Tangoganizani, chiwalo chokumbidwa chimenecho chiripo panobe, patapita mamiloni a zaka.”

56 Ine ndinaganiza, “O,” ine ndinati, “M’bale Cox, idzakhhalapo nthawi pamene chiwalo chokumbidwa icho sichidzakhhalaponso. Sipadzakhala pali mthunzi umodzi wa icho. Koma chifukwa Iye anawuka kwa akufa, ine ndidzakhala moyo ndipo inu mudzakhala moyo, kwa nthawizonse, ndi kwa mibadwo yosawerengeka.”

57 Pamene ziwalo zokumbidwa zonse zidzakhala zitazimirira, ndipo nthawi yonse ya ukalamba itapita kale, ndipo mithunzi itagwa, ife tidzakhhalabe moyo, tidzakhala ndi kukhalabe, kwa nthawizonse. Chifukwa, pa kuvomereza chiwukitsiro cha Ambuye Yesu Khristu, ife timakhala zinthu zachisavundi, tikubuula mu Mzimba, kuyembekezera nthawi ya chiwombolo chathu, kuti ifenso tidzakhala ndi Iye mu Kukhalapo Kwake kodala, kukhala moyo kwa nthawizonse. Ndi chododometsa bwanji! Palibe chodabwitsa icho chimakondoweza mitima ya anthu! Palibe chodabwitsa icho chawafikitsa anthu poti zipembedza.

58 Palibe chodabwitsa kuti anthu lero angakhoze kumakwawa pa maondo awo, ndi kumakhudza miyala, ndi kumasisita mitanda, ndi—ndi zina zotero, chifukwa, chinachake mkati mwa iwo, chinachake pansu pa solo ya munthu chiri kulirira ku chinachake chimene iwo sangakhoze kuchipeza. “Chakuya kuyitanira ku Chakuya.” Ndipo ngati pali chakuya, chikuyitanira, pamenepo kuyenera kukhala Chakuya kuti chiyankhire kwa icho. Apo payenera kukhala basi.

59 Motsimikiza monga dzuwa lofunda limasambitsa kudutsa minda, pamene iyo ili yowawulidwa ndi kuzizira kwa dzinja, payenera kukhala kuli . . . Dzuwa limenelo linaikidwa pano kwa chinachake. Pansi mkati umo, penapake, zosawoneka kwa diso laumunthu, pali mmera ndi moyo, umene uti udzaphuke kachiwiri chifukwa kuti dzuwa linatumizidwa pa cholinga icho chomwe.

60 Ndipo motsimikiza basi monga Kuwala kwa Mwana wa Mulungu kumasambitsa mu mtima wa munthu, pali kakang’ono kobisika kenakake mmenemo kamene munthu sangakhoze kukafotokoza. Iko kakuyitana momveka. Payenera kukhala pali, penapake. Ine ndikamaganiza za izo, ndipo mtima wanga umanjenjemera ndi chisangalalo, podziwa kuti ife tiri nawo

umboni wapamwamba lero kuti Khristu anawuka kwa akufa, tsopano.

⁶¹ Ndipo ine ndikaganiza za nthawi za Chipangano Chakale, naponso, pamene iwo ankayang'anira ku kudza kwa Ambuye Yesu, pamene iwo anamuwoneratu Iye ndipo anapembedza, pa lingaliro lomwe la izo. Panali chinachake mwa iwo, chikuitanira, “kuya kukuitanira ku Kuya,” kuyembekezera nthawi, kuyang'anira nthawi pamene Yesu akanati adze.

Tsopano, lero, Iye atabwera kale. . .

⁶² Tsopano, mmbuyo uko, Satana anayesera kuti achititse khungu maso a iwo amene ankayang'anira kwa izo, kuti awawuze iwo kuti panalibe zoterozo. Koma, mwanjira ina kapena imzake, kupyola chirichonse chimene ife tikanakhoza kunena mmawa uno, koma monga Mzimu Woyera unakankhira pa mtima wawo ndi kuwapatsa iwo njala ndi ludzu, kuti panali kudza Mmodzi Wolungama.

⁶³ Yobu, tsopano taganizani, zaka zikwi zinai. . . Zaka zikwi zinai kudza kwa Ambuye Yesu kusanachitike, Yobu anawona chiwukitsiro. Ndipo pamene iye anachiwona icho mwa masomphenya, kuti icho chikanati chidzakhale, zaka zikwi zinai izo zisanachitike, iye anali nacho chitsimikizo, kuti, “Ine ndikudziwa Muomboli wanga alimoyo, ndipo pa masiku otsiriza Iye adzaima pa dziko lapansi. Ngakhale mphutsi za thupi ziwononge thupi ili, komabe mu thupi langa ine ndidzamuwona Mulungu; Yemwe ine nditi ndidzamuwone mwiniwanga; maso anga adzamupenya, ndipo osati wina.” Panali chakuya, chikuitanira ku Chakuya, mwa Yobu.

⁶⁴ Satana akanakhoza kuyesera kuti achifutepo icho ndi imfa. Iye akanakhoza kunena, “Inde, Yobu, iwe ukupita mmanda. Mphutsi za thupi zitenga thupi lako.” Uko nkulondola. Ife tikudziwa izo.

⁶⁵ Koma Yobu anati, “Ine ndidzaima pa masiku otsiriza ndi Iye.” Iye anali nacho chitsimikizo kuti Iye akanati adzakakhale kumeneko, pakuti munali chinachake mwa Yobu chimene chinamuza iye izo. Ndipo pamene Satana anayesera mwakukhoza Kwake kuti afute icho ndi imfa ndi chirichonse, Yobu ankayang'anira kwa icho, kuti achiwone icho. Anafa mwa chikhulupiro, anapereka mzimu; anawuka kachiwiri pa mmawa wa Isitara, ndi Khristu, ali wachisavundi pakati pa anthu lero! Aleluya! Zindikirani. Palibe zodabwitsa Zinthu Zaungelo zikhoza kuimba, “Aleluya!” Kudziwa!

⁶⁶ Tsopano, lero, pakhoza kukhala ena, ife tikhoza kuisita mitanda, ife tikhoza kuisita mafupa a anthu akufa; ndi mitima ya anthu ikuitana kufuna chinachake. Iwo ali. Muli chinachake mkati mwao, chimene chikuwoneka kuti chiri. . . Pokhala anthu, iwo amafuna. . . Iwo amadziwa kuti pali chinachake, penapake, chachikulupo kuposa chimene iwo chirichonse

chimene amachidziwa, ndipo iwo akufufuza icho, kuchifufuza icho. Ndipo iwo akuyesera kuti achipeze icho pa kupembedza mafupa a anthu akufa, pa kususita mitanda, pa kumanga matchalitchi aakulu.

⁶⁷ Koma, o, ku chiyembekezo chodala icho lero, ku chitsimikizo chodala icho, kuti munthu aliyense yemwe anayamba wabwerapo pokhudzana ndi chiwukitsiro, amadziwa, kupitirira mthunzi uliwonse wa kukaikira, kuti Khristu wauka kumanda, ndipo ife tinawuka ndi Iye. Iye tawuka ndi Iye, mmawa uno. Kuti, powona, izo siziri ayi. . .

⁶⁸ Ndi njala, mmodzi aliyense wa inu kubwera kwa Khristu. Inu musalandire Mzimu Woyera, inu munachitira njala ndi ludzu. Inu munayenda. Inu munafunafuna. Inu munawerenga Baibulo. Inu munalira. Inu munachita chirichonse chimene chikanakhoza kukhalapo. Inu mwina munabwereza rozare. Inu mwina munabwereza mikanda. Inu mwina munachita mitundu yonse ya machitidwe achipembedzo. Inu mwina munasiya kudya nyama. Inu mwina munasunga masiku a sabata. Inu mwina munachita zinthu zonse izi za chipembedzo zimene dziko limazikamba lero.

⁶⁹ Koma, pamene nthawi imodzi imene inu munayamba mwadzipereka ku mtanda, apo panadza chiwukitsiro. Izo zimakupatsani inu chitsimikizo, cha, “Ine ndikudziwa Muomboli wanga alimoyo lero!”

Chitsimikizo chodala, Yesu ndi wanga!
O, kulawiratu kwake kwa ulemerero Wauzimu!
Wolowa wa chipulumutso, wogulidwa ndi
Mulungu,
Wobadwa ndi Mzimu Wake, wotsukidwa mu
Magazi Ake.

⁷⁰ Ndiyo nkhani yabwino. Ndiwo malamulo a aliyense. Ndiko kutumidwa kwakukulu, kuti ife tiyenera “kupita mu dziko lonse, ndi kukalalikira Uthenga uwu.” Kuwupereka Iwo kwa anthu, “mu mphamvu ya chiwukitsiro.” Tsopano, ndikudalira kuti. . .

⁷¹ Tsopano, nthawi yathu yangotsala pang’ono kuti ithe, kwa kuyankhula kwapang’ono kwa mmawa kuno palimodzi. Ife tikuti tilalikire tsopano, mwa pafupi maora angapo, kuti tibwerere kudzalalikira msonkhano wa Isitara lero.

⁷² Koma, lero, mu kuyankhula kwakung’ono uku, ndi kumverera kodabwitsa bwanji! Ndi chiyanjano chodabwitsa bwanji palimodzi! Ndipo ine ndikukhulupirira ndi mtima wanga wonse kuti, lero, kachisi wakale wamng’ono uyu awona umboni wolunjika kuti Yesu Khristu anawuka kwa akufa, akuwoneka patsogolo pa maso awo; Mulungu akuchiritsa odwala, ndi kuchita zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa zimene kutumidwa kwakukulu kunaikaponso. Chitetezero chachikulu chimene

chinapangidwa pa Kalvare chinaikaponso zinthu izi. Ndipo, kwa ine, ndi chitsimikizo chosalephera cha chiwukitsiro Chake.

⁷³ Iye atawuka kale kwa akufa, Iye anati, “Inu muyenera kuti mupite ku dziko lonse ndi kukalalikira Uthenga uwu kwa cholengedwa chirichonse. Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.”

⁷⁴ Ndipo inu mukhoza kukhala nao makafiduro onse, ndi kutikita konse, ndi zirizonse zonse zimene inu mukuzifuna. Koma ndipatseni ine Mphamvu ya chiwukitsiro, kuti ine ndizikhoza kumawaona Ambuye Yesu lero, monga Kakombo wa Mchigwa ndi Nyenyezi ya Mmawa. Izo zimasindikiza izo, kwa ine. Ndiyeno ine ndikhoza kunena, ndi Yobu wakale, “Ine ndikudziwa Muomboli wanga alimoyo.”

Nchiani chingatsuke machimo anga?
Sichina koma Magazi a Yesu.

⁷⁵ Nchiani chingandipange ine wamphumphu kachiwiri, ku matenda alionse, chirichonse, msinga iliyonse imene ine ndinayamba ndakhalamo? Sichina koma Magazi a Yesu, ndi Mphamvu ya chiwukitsiro Chake. Ndi chinthu chopambana bwanji! Ine ndimamukonda Iye. Sichoncho inu? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Lidalitsike Dzina Lake loyera!

⁷⁶ Tsopano, kodi Yobu anali wokhumudwitsidwa? Kodi Yobu anasiyidwa kunjira chifukwa ankakhulupirira izi? Palibe. Palibe. Kodi Yobu anapusitsidwa, pa chimene iye anawona, vumbulutso lake? Kodi chakuya, poitanira ku Chakuya, zinamunyenga Yobu? Ena akanakhoza kulingalira izo mu tsiku lake. Koma, o, izo zinafika motani pa mapeto? Ndipo Yobu, pamene iye anafa, atakhala munthu wachikulire, Mulungu anamudalitsa iye mu moyo.

⁷⁷ Ine ndikukuuzani inu, inu mumupenye munthu aliyense yemwe inu mukufuna kutero. Mvetserani kwa izi, inu anthu a mkachisi, ndi inu alendo muli ndi ife. Moyo uliwonse umene inu mukukhala, ndi moyo umene inu muti mudzakolole. Inu, basi monga inu mumafesa, inu mumakolola. Ine ndinali usinkhu wa zaka makumi anai ndi zisanu ndi chimodzi, tsiku lina. Mulungu wandirola ine kukhala moyo wotalika mokwanira kuti ndiwone kuti iwe sungakhoze kuchita cholakwika ndi kudutsa nacho.

⁷⁸ Iwe uyenera kuti uzichita chinthu cholondola, chifukwa Khristu wauka kwa akufa ndipo maso Ake ali pa Mpingo, ndipo Iye amauyang’anira Iwo ndi kuwutsogolera Iwo. Musati konse muzipita motsutsa kumverera kwa Mzimu Woyera pamene Iye akuuzani inu kuti muchite chinachake. Ziribe kanthu zimene dziko likunena, inu muzichita zimene Iye anena kuti muchite. Iye nthawizonse amatsimikizira Choonadi ndi kuchisunga Choonadi mowongoka.

79 Tsopano, pamene iye...pamene mneneri wamkulu uyu wa Ambuye, Yobu, pamene iye anafa ndipo anaikidwa. Kukhomerera pang'ono kokha tsopano kwa chimene . . .

80 Ine ndikufuna kuti ndiwubweretse msonkhano waung'onowu ku kutseka tsopano, chotero ife tikhoza kufulumirira kunyumba, ndi kukabwerera kachiwiri ku msonkhano waukulu wamachiritso. Ine basi . . .

81 Ine si wotentheka. Inu mukudziwa ine sindiri. Kapena, ngati ine ndiri, ine sindikudziwa izo. Koma ine ndikungomverera Chinachake patali mmusi mwa ine, chikukankha ndi kukanikiza. Ine ndikungokhulupirira kuti ife tikuyang'anizana ndi chinachake chachikulu, mmawa uno, kwa ulemerero wa Mulungu. Ine ndikukuuzani inu, ine sindikanati. . . O, mai! Chiani. . . Kudziwa chinthu chachikulu ichi, kuti Khristu ali moyo lero! Kuti, kuzungulira dziko lonse, konsekonse, ndi chipembedzo chirichonse, chirichonse chimene chiripo, ziribe kanthu chimene, gulu lonse likanati lichitembenezire Icho pans; komabe, kwa ine, Iye ali moyo. Iye ali moyo.

Ndiye, ife tkuwona ngati anthu akhumudwitsidwa, amene amakhulupirira Zimenezozo.

82 Yobu, pamene iye anafa, iye anaikidwa mu—munda uko. Ndipo manda ake anasungidwa.

83 Ndiyeno pamene potsatira kunabwera aneneri akale, Abrahamu. Okoma mtima amu Baibulo, Abrahamu ndi Sara. Pamene Sara anafa, Abrahamu anagula kagawo ka dziko pafupi kumene Yobu anaikidwa, ndipo anamuika Sara. Iye anati, “Ine ndine wolowa molumikizana ndi inu kutsidya uko.” O, mai! Ine ndikuzikonda izo, “Olowa limodzi!”

84 Ndi momwe, lero, ena a iwo amati, “Chabwino, M'bale Branham, inu mukutanthauza kuti inu muwusiya mpingo wa Baptisti? Inu mukachita *izi, izo*, kapena *zinazo*?”

85 Ine ndine wolowa limodzi ndi “oyera-odzigudubuza” awa, ndipo ine—ine ndikufuna kuti ndikhale ndi iwo. Ine. . . Kuti, monga Rute anati, kalelo, “Kumene iwe. . . Anthu ako ndi anthu anga. Mulungu wako ndi Mulungu wanga. Kumene iwe uti ukafere, ine ndikafera. Kumene iwe uti ukaidwe, ine ndikaikidwa.” Ine ndikufuna kuti ndife kwa ndekha, kwambiri chotero, mpaka ine ndikhale munthu watsopano mwa Khristu Yesu.

86 Chotero, iwo anamuika Yobu. Ndipo Abrahamu anamuika Sara pafupi kumene ndi malo ake. Chinachake mwa iwo; kununkhiza kumeneko!

87 “Chabwino,” inu mukuti, “tsopano, kodi chiripo chinthu choterocho, M'bale Branham? Tsopano, inu munali kupitirira, pa za zipembedzo zosiyana. Iwo ankawerenga izo kuchokera

mu bukhu, nawonso.” Uko nkulondola. Iwo ankawerenga izo kuchokera mu mabuku.

⁸⁸ Koma Uku si kuwerenga kuchokera mu bukhu. Ili ndi Bukhu likupangidwa mowonetseredwa. Awa ndi Mawu. Mbewu ikuyamba kukula, ndizo, “Ine ndikudziwa.” Ngati inu mutangowerenga kalata, inu munena kuti, “Ine ndikuyembekeza chomwecho. Ine ndikukhulupirira chomwecho.” Koma pamene mbewu yabweretsa Moyo, ndiye inu mumadziwa chomwecho. Amen. Amen. O, ndizo “ndikudziwa chomwecho.”

⁸⁹ Yobu ankati, “Ine ndikudziwa!” “Ine ndayembekezera izo; ine ndakhulupirira mwa izo; ine ndapanga nsembe; ine ndachita zinthu zonse izi; ine ndayembekezera chomwecho.” Koma pamene masomphenya anabwera, ndipo iye anawaona iwo, iye anati, “Ine ndikudziwa izo.” Chinachake chachitika.

⁹⁰ Inu mukhoza kumapita ku mpingo. Inu mukhoza kunena Tizikhulupiriro tonse ta Atumwi. Ndipo inu mukhoza kuchita zinthu zina zonse izi zimene ziri zachipembedzo. Inu mukhoza kubatizidwa mwa mawonekedwe aliwonse amene inu mukufuna kuti mubatizidwe. Inu mukhoza kuchita chirichonse cha zinthu izi zimene inu mukufuna kutero. Koma mpaka moyo wanu utakhala woukitsidwa ndi chiwukitsiro cha Ambuye Yesu, inu. . . “Ziyembekezo” zonse zitachoka pamenepo, ndipo “ndikudziwa chomwecho” atabwera umo. “Ine ndikudziwa!”

Yobu anati, “Ine ndikudziwa kuti Muomboli wanga ali moyo.”

⁹¹ Abrahamu anati, “Ine ndinali ndi mtundu womwewo wa masomphenya. Pamene ndinali patali pa phiri, pamene (Khristu) Mulungu anakomana ndi ine, ndipo anandipatsa ine. . . maina Ake achiwombolo, monga Yehova-yire, Yehova-rafa, ndi onse awo; kuwona imfa, kuikidwa, ndi chiwukitsiro. Kuziwona izo, ndipo ine ndinazipereka izo mwa mwana wanga yemwe, pamene ine ndinamuwona Isaki wamng’ono. Amake a uyu, (amake atafa apa), mnyamata wao. Pamene ine ndinamutengera iye pa phiri, kumusiya iye kunyamula nkhuni zake zomwe, kukwera pamwamba pa phiri,” Genesisi 22, “ndipo pamenepo iye. . . ine ndinamugoneka iye pa guwa ndipo ndinkati ndiutenge moyo wake womwe. Podziwa kuti ine ndinali nditamulandira iye monga wochokera kwa akufa, ine ndimakhulupirira kuti Iye akanati amuwukitse iye kachiwiri. Ndipo mwa chiyembekezo chachikulu ichi chimene chimagunda mu mtima mwanga, ine ndikudziwa Iye anati Iye akanakhoza kumuwukitsa iye.” Mukuona? Iko kunali kuwoneratu kwa chiwukitsiro; chinthu chomwecho Yobu anali nacho.

⁹² Chotero iye anati, “Tsopano, ine ndine wolowa limodzi ndi Yobu, chotero ndiyikeni ine mu nthaka yomweyo.” Ndiko kulondola. Chotero iwo anamutengera iye cha kumeneko, anamutengera Sara kumeneko ndipo anamuika iye pafupi ndi

Yobu pomwe. Abrahamu anati, “Tsopano pokhala kuti iwo. . . Malo awa akhoza kugulitsidwa kwa winawake, kapena chifukwa inu munawapereka iwo kwa ine. Ine sindikufuna kuti inu mundipatse iwo kwa ine. Ine ndikufuna kuti ndilipirire iwo. Ngakhale inu mwawapereka iwo kwa ine, ine ndikufuna kuti ndilipirire iwo.”

⁹³ Ndipo ndi momwe, munthu aliyense, ndimo, “Mwa chisomo inu munapulumsidwa, osati mwa ntchito,” palibe chimene inu mungakhoze kuchita. Koma ngati inu munayamba mwalandirapo chiwukitsiro chodala mu mtima mwanu, inu mukufuna kumakhala moyo wa Chikristu, chokhumba chonse cha moyo mwa inu ndi kuti muzichita icho chimene chiri cholondola. O, ine ndikungozikonda izo! Izo siziri kuti inu muli okakamizika kuti muchite *ichi*. Osati kuti muli okakamizika, koma muli Chinachake mwa inu chimene chimakupangitsani inu kufuna kuchita izo. Inu mumafuna kuti muchite izo. Inu simumachita izo chifukwa ndi ntchito. Inu mumachita izo chifukwa cha chikondi.

⁹⁴ Inu mumati, “Ine ndikudziwa. Chabwino, ine ndiyenera kuti ndiwuke ndi kuwakonzeketsera ana kuti azipita ku tchalitchi mmawa uno. O, mai!” Mukuona? O, mai! Inu simunayambe mwakhudzapo chiwukitsiro.

⁹⁵ M’bale, pamene chiwukitsiro chibwera mu mtima wanu, inu mumakhumba kuti muchite izo. Pamakhala chinachake, chimene iwe sungakhoze kudzikhalitsa kutali ndi icho; Chinachake mkati.

⁹⁶ Yobu, pamene iye anawona ichi! Ndipo Abrahamu anachiwona icho; iye anamuika Sara pafupi ndi Yobu. Anagula mundawo, anawugula iwo ndi ndalama zake, kuti iwo ukhale wotetezedwa. Kuika mboni pamaso pa iwo, kuti iye akhale otsimikiza kuti iye anagula munda uwu kuti akhale malo a manda. Ndiyeno, Abrahamu mwiniwake, pamene iye anafa, iye anakaikidwa ndi iwo, aponso, mu munda womwewo.

⁹⁷ Abrahamu anabala Isaki. Ndipo pamene Isaki anafa, iye anakaikidwa ndi Abrahamu; pa masomphenya omwewo, lingaliro lomwelo, “chakuya kuitanira ku Chakuya,” chomwecho “ine ndikudziwa Muomboli wanga ali moyo” yemweyo. Chinthu chomwecho, umboni womwewo.

⁹⁸ Ndiyeno pamene Isaki anabala Yakobo. Ndipo Yakobo atamwalira, kutali komwe mu Igupto, kutali uko ndi dziko ili.

⁹⁹ Ndipo iye anali munthu wolumala. Iye ankayenda mosiyana ndi mmene iye ankayendera, chifukwa usiku wina iye anafika pokhudzana ndi Mngelo wa Mulungu. Ndipo Ambuye anamugwira ntchafu yake ndipo anamupanga iye kumayenda mosiyana. Iye anali nawo umboni kuti iye anali atagwiridwa ndi Mulungu, ndipo Mulungu anali atamugwira iye. Ndipo ndi momwe, pamene iye anali nao umboni umenewo, ntchafu

yokalamba yolumala iyo imene iye ankayenda nayo pamenepo, kumupanga iye kuti aziyenda molunjika.

¹⁰⁰ Mbali imodzi, wodzitama kwambiri, kwambiri... Chabwino, chimene iye anali kutchedwa kwenikweni, iye anali wachinyengo. Iye ankatchedwa “wachinyengo.” Mawu omwe akuti *Yakobo* amatanthauza “wachinyengo.” Ndipo pamene iye anali pa mbali iyi, wachinyengo; wamkulu, wathanzi, wamphamvu, wachinyengo.

¹⁰¹ Pa mbali inayo, kalonga wotsimphina amene anakhala ali ndi Mulungu; wogwiridwa, wosiyana, ali nacho chiyembekezo chodala chimenecho mkati mwa iye! Iye ankayenda mosiyana. Iye ankachita mosiyana. Iye ankakhala moyo mosiyana.

¹⁰² Ndipo pamene iye anali kukonzekera kuti afe, kutali komwe mu Igupto. Taganizani za izo tsopano. Ndi kudzoza kumeneko chisanachitike chiwukitsiro, zinaperekedwa kwa iye mwa muyezo, chisanachitike chiwukitsiro. Iye anati, “Ine ndikudziwa chinachake chidzakachitika kutali uko mu Igupto, mmodzi... osati mu Igupto; koma uko mu dziko lolonjzedwa, limodzi la masiku amenewa. Chotero pa malo awo omwe kuti kudzoza uku... Bwera pano, mnyamata wanga, Yosefe,” yemwe anali mneneri. Iye anati, “Bwera kuno ndipo ika dzanja lako pa iyi, ‘analimbana,’ malo amene ine ndakhala ndiri. Ndipo ulumbire kwa ine, mwa Mulungu wa Kumwamba, kuti iwe sudzandiyika ine kunoko. Lumbira kuti iwe sudzandiyika ine kuno.” Pakuti, iye ankadziwa kuti zinali zofunikira kuti iye adzasonkhanitsidwe ndi anthu amenewo.

¹⁰³ Ndicho chifukwa, lero, ife timafuna kuyimba pamene ife tiyika dzanja lathu pa mtanda wokhukhuluzidwa wakalewo, “Ine nditenga njira ndi onyozedwa apang’ono a Ambuye; ngakhale Iyo ikhale ikutsutsidwa, ngakhale Iyo ikhale ikusekedwa, ngakhale ine ndikhoze kukhala mnyamata wamkulu, wotchuka kuno.”

¹⁰⁴ Monga choncho, tsiku lina, monga zinali, mnyamata wamng’ono wakale cha ku tawoni kuno, ndi wokhala ngati wotchuka pakati pa... ena otero, anthu achinyamata. Koma ine ndinawona chinachake tsiku lina, chimene chinafika pansu mkati umu. Ndipo ine ndinatenga malo a mbali yotsimphina, pa mbali inayi.

¹⁰⁵ Kodi sindinu okondwa, mmawa uno, inu munatenga malo anu kumeneko? Pakuti munali chinachake mu—mwa inu! [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

¹⁰⁶ Dona wamng’ono... Pamene ine ndinali mlaliki wa chinyamata chabe, kuno ku malo kumene ine ndinali kulalikirira, iye... ine ndinamutengera iye ku tchalitchi usiku wina. Iye anati, “Billy, ife tidza... tikatha ku tchalitchi, kodi ife tingakhoze kupita ku kanema?”

Ine ndinati, “Ine sindimapita ku makanema.”

107 Iye anati, “Chabwino,” anati, “tingakhoze ife—tingakhoze kukhala ku—kupangana, kapena tsiku, kuti tidzapite ku zovina zina zomwe zinkati zikhalepo?” Ndipo msungwanayo anali mphunzitsi wa Sande sukulu.

108 Ndipo ine ndinati, “Bwanji, ayi.” M’bale wake anali mlaliki. Iye samakhala kutali kwambiri kuchokera pano pomwe. Ndipo iye. . . Anati, “Kodi ife tingakhoze kupita ku—ku—kukavina?”

Ine ndinati, “Ine sindimavina.”

109 Ndipo iye anati, “Iwe sutero?” Anati, “Nkuti kumene iwe umakakhala ndi kusangalala kulikonse?”

Ine ndinati, “Ubwere uko ku tchalitchi, ine ndikakusonyeza iwe.” Ameni.

110 Ine ndikukuuzani inu, m’bale, pamene ine ndimverera mphamvu ya chiwukitsiro imeneyo, yosintha ya Ambuye Yesu Khristu ikuzungulira kudutsa mu thupi la umunthu, imapereka chitsimikizo changwiro icho, muli chisangalalo chochuluka mwa Iyo, mu maminiti asanu, kuposa chimene chiripo mu chisangalato chonse cha chidziko chimene chingakhoze kuperekedwa. Mphamvu yowukitsidwa ija!

111 Chabwino, usiku umenewo, ochimwa anabwera ku guwa. Iye anali atakhala mmbuyo umo akulira, nayenso. Ine ndinati, “Tsopano, taona, mlongo, iwe ukuona kumene chisangalalo changa chiri?” Ine ndinati, “Ine ndiri wokondwa pakali pano kuposa zinthu zonse zimene inu ungakhoze kupereka mu dziko. Dziko, ndi mphamvu zake zonse, sizikanakhoza kutenga konse malo a Ichi.” Kuwona miyoyo ikubwera, muli Chinachake mmenemo!

Anati, “Chabwino, ndi chiyani icho? Iyo si ntchito yako konse.”

112 O, inde, iyo ili, nayonso. Ndi ntchito ya mwamuna aliyense ndi mkazi yemwe ali wobadwa ndi Mzimu wa Mulungu, kuti aziona Akhristu akubwera mu Ufumu wa Mulungu. Ndi udindo wanu. Ndi ntchito yanu. Ndipo ndi chisangalalo bwanji icho chiri pamene izo zonse zikuchitika, pamenepo, inu mumaona mtendere wake. Inde.

113 Yakobo anati, “Tsopano ika dzanja lako apa, ndipo ulumbire kuti sudzandiyika ine kuno.” Chotero iwo anamutenga iye ndipo anakamuika iye kumtunda uko ndi onse a iwo.

114 Ndiyeno—ndiye, Yosefe, izo zinakhala ngati zinabwera kuchokera kwa Yakobo mpaka kwa Yosefe. Ndipo pamene Yosefe anafera uko mu Igupto, iye anati, “Tsopano, penyani, musati muniyike ine kuno chifukwa ine ndikudziwa tsiku lina ife tidzachokako kuno. Chotero, ine. . . Inu mungosiya mafupa anga panja pa nthaka.” O, mai! “Ine ndikufuna kuti ndipereke umboni uliwonse umene ine ndingakhoze, kuti ine ndikukhulupirira mu izo.” Ndiko kulondola. Anati, “Ndikadzakhala ine nditafa,

mudzangosiya mafupa anga pamenepo mwa umboni.” Mukuona? Ndi chiyani icho? Iye akanakhoza kunena zochuluka kwambiri monga Yobu, “Ine ndikudziwa Muomboli wanga alimoyo,” pakuti iye anali atachiwona chinthu chonsecho chikuchitidwa seweru. Iye anali atawona, monga Yobu.

¹¹⁵ Yobu anaziwona izo mu masomphenya. Abrahamu anawona izo mwa Isaki. Ndipo Isaki yemwe... ndipo Yakobo, ndi ena otero. Ndipo Yakobo anali ataziwona izo pa kulimbana.

¹¹⁶ Tsopano Yosefe anaziwona izo ndi moyo wake womwe. Iye anawona kuti iye anali atabadwa mnyamata wododometsa, kuti iye anali mpenyi. Panali chinachake ndi iye; iye ankakhoza kumawona masomphenya. Iye sankakhoza kuwamvetsa iwo. Iye anapita ngakhale ndipo anakawona... Anakawawuza amayi ake ndi abambo, pamene iwo anayesa kumukonza iye, pamene iye anawona mitolo yonse ikuweramira pa wake. Iye sankakhoza kuzimvetsa izo. Komano, chinthu chotsatira, iye anapeza kuti iye anaperekedwa ndi abale ake. Iye anati, “Kodi ine ndikuwonetsera chiani pano? Kodi ndi kudziwidwiratu kotani uku kumene ine ndikukulandira?” Iye anawuyang’ana moyo wake womwe.

¹¹⁷ Ndipo munthu aliyense ukhoza kuyang’ana moyo wako womwe ndipo ungakuwuze pafupi chimene iwe uli, ngati iwe utangodzifufuza pawekha, ngati iwe uli Mkhristu weniweni kapena ayi. Kupenya zinthu zimene iwe umachita, ndi zimene iwe umanena, ndi oyanjana nawo ako, ndi zina zotero. Iwe upeza ngati uli nacho kwenikweni chirichonse pamenepo, kapena ayi.

¹¹⁸ Iye anawuwona moyo wake pamene iwo unayamba kusuntha. Ndipo chinthu chotsatira inu mukudziwa, iwo anapeza kuti iye anaponyedwa mu dzenje; ananyengedwa ndi abale ake, kuganiziridwa kuti waphedwa ndipo anaponyedwa mu dzenje, ndipo anachotsedwamo kachiwiri. Yosefe anaziwoneratu izo. Iye anadziwona yekha ali mu ndende. Iye anadziwona yekha ali mu nyumba ya mdima. Iye anamuwona Mulungu ali ndi iye, chirichonse chimene iye ankachita, ngakhale. Iye anali kalonga wa kulemera. Dziko linalamera. Kulikonse kumene Yosefe anali, kunali kulemera, pakuti iye anali kalonga wa kulemera. Ndipo, iye, anawonetseratu Khristu.

¹¹⁹ Kulikonse kumene kuli Khristu, kumakhala kulemera. Ndipo pamene Khristu azidzabwerera ku dziko lapansi, themberero lonse la dziko lapansi lidzachotsedwapo, ena a masiku awa. Chipululu chakale chidzaphuka ngati duwa, ndipo malo okumbika adzasalazidwa. Ndipo ilo lidzabala mochuluka, pakuti Iye ndi kalonga wakulemera, kulikonse kumene Iye ali. Aleluya! Kalonga wa kulemera!

¹²⁰ Momwe ife tingakhoze kukhala pa izi kwa pafupi ora pakali pano! Koma, kuti tifulumire tsopano, ife tiyenera kuti tifulumire.

¹²¹ Tsopano tayang'anani pa Yosefe, kuziwona izo apo, pamene iye ankadziwa kuti chirichonse chimene iye ankachichita. Iye anawawona abale ake amene anamupereka iye, potsiriza akubwera kwa iye, osamudziwa yemwe iye anali; ndi kugwada patsogolo pa iye, molemekeza. Ndipo iwo amene anali atamupachika iye, monga izo zinaliri, anamuponyera iye mu nthaka, iwo amene anali atamugulitsa iye kwa Aigupto, onse amene anamuchitira moipa iye, anaima patsogolo pa iye. Ndipo, iye, kalonga wamkulu; ndipo iwo ananjenjemera. Ndipo iwo anati, "O, izo..." Ananjenjemera, chifukwa, anati, "Ifi tinamupha m'bale wathu." Ndi zonse za izo, ndipo momwe izo zinali zoti zikhale mwa mthunzi wotsogolera.

¹²² Yosefe, iye anadziwa kuti izo zikanati zidzakhale zikhaliidwe za dziko pa kudza kwa Ambuye Yesu, chotero iye anatchula za mafupa ake. Iye anati, "Musati mundiyike ine kuno. Koma ine ndikufuna kuti ndikhale moyo umboni uliwonse umene ine ndingakhoze, kuti ine ndikuhulupirira kuti tsiku lina kudzakhala chiwukitsiro, kutali uko, kumene iwo amene anali nako kudzoza komweko anapitawo."

¹²³ Ndipo chotero ukhoza Mpingo kunena, mmawa uno! Ngakhale "motentheka," monga ife timatchedwa; ngakhale chifukwa ife timakhulupirira mu Mphamvu ya chiwukitsiro; ngakhale ife timakhulupirira mu machiritso Auzimu ndi zizindikiro zonse zauzimu zimene Khristu anazilonjeza; ife tinachita kutenga mbali ya "osaphunzira," kapena "otentheka," ndi zina zotero! Sizikupanga kusiyana kulikonse chimene ife tiyenera kuchitenga, malingana ngati ife tikudziwa kuti Muomboli wathu alimoyo, ndipo wabweretsa umboni mu mtima mwathu, kuti Iye alimoyo ndipo akulamulira.

¹²⁴ Yosefe anati, "Ine ndikufuna kuti ndipange umboni uliwonse momutsutsa Mdierekezi womwe ine ndingakhoze."

¹²⁵ Chotero iye anaponyera mafupa ake panja apo, ndipo iwo anagona pamenepo kwa zaka mazana anai. Ameni. Pakuti, iwo amayang'ana kupyola zimenezole Anthu amati, "Ndi wotentheka bwanji!" Izo zinkawoneka ngati, pamenepo, wotentheka, koma izo zinatsimikizira kuti ndi Choonadi. Ameni.

¹²⁶ Chotero izo zidzakhala kwa aliyense yemwe ali nacho chiyembekezo chodala ichi cha nkhani iyi mmawa uno, "Ine ndikudziwa Muomboli wanga alimoyo. Ine ndikudziwa izo, ziribe kanthu chiani!"

¹²⁷ Iwo amati, "O, ife tikulemera kuno. Igupto yense akulemera pamene ife tiri kuno," zinthu zonse izi.

¹²⁸ Koma izo sizinapange kusiyana kulikonse. Iye ankadziwa kuti iwo anali woti adzatulukeko kumeneko, motsimikiza basi

monga dziko. Iye anati, “Tsopano, mudzatengere mafupa anga kumeneko, ndipo mudzakawaike iwo mu Igupto. . . uko mu dziko lolonjzedwa, uko mu dziko la Kenani, kuchokera ku Igupto.” Chotero pamene iwo. . . Mose anabwera umo, mneneri wina wodzozedwa, ndipo iye anatenga mafupa a Yosefe, ndipo anawatengera iwo uko ndipo anakawaika iwo mu munda womwewo, malo omwewo pamene onse a iwo anakaikidwako. Iye anatenga njira yake, ndi onse a iwo. Chifukwa? Munali Chinachake mwa iye. Chinachake mwa iye! Ziribe kanthu. . .

¹²⁹ Inu simukuwamva anthu ena onse kumusi uko akunena chirichonse za izo. “Chabwino, paliponse mpabwino.” Iwo amangogwera paliponse pamene iwo angafune.

¹³⁰ Koma munali Chinachake mwa iye, Chinachake chimene chinali ndi masomphenya omwewo amene Yobu anali nawo, masomphenya omwewo amene onse a iwo anali nawo. Ziribe kanthu chomwe dziko lina lonse linkaganiza, zimene iwo ankachita, izo zinalibe kanthu kochita ndi Yosefe; izo zinalibe kanthu kochita ndi Abrahamu, ndi Isaki, ndi Yakobo, ndi ena onse a iwo. Chinachake chinkakankhira ku dziko lolonjzedwa ilo. Zinkawoneka motentheka, koma iwo ankafuna izo chifukwa panali Chinachake mwa iwo. “Chakuya chikuitanira ku Chakuya.”

¹³¹ Ndi momwe ziriri lero ndi wokhulupirira aliynse. Pali Chinachake mwa iwo, chimene chimakanikizira kwa Icho. Ziribe kanthu, iwe ukhoza kuyesera *ichi*, *icho*, kapena *china*, koma pali Chinachake chimene chimakanikiza. Iwe umadziwa, kupyola mthunzi wa kukaikira, kuti kuli Mzinda Wowumanga wake ndi Wowupanga ndi Mulungu. Iwe umadziwa kuti kuli Chinachake uko, chotero iwe umakanikizira ku Icho.

¹³² Tsopano, pa tsiku limene iwo anamuika iye, mafupa kumeneko, mazana a zaka atadutsa.

¹³³ Ndipo potsiriza, tsiku lina, “Kwa ife Mwana wamwamuna anabadwa, kwa ife Mwana anaperekedwa. Ndipo Dzina Lake adzamalutcha Wodabwitsa, Wauphungu, Mulungu Wamphamvu, Kalamu wa Mtendere, Atate wosatha.” Ndipo Iye anabwera ku dziko lapansi, ndipo Iye anabwera mwa njira ya kukhola, wosauka ndi wotsikitsitsa.

¹³⁴ Koma Chinachake mwa Iye, chimene chinkadziwa! Iye anaimea pamenepo ndi uneneri umodzi wochokera m’Baibulo. Iye anati, “Inu muphwasule thupi ili, ndipo mu masiku atatu Ine ndidzaliwukitsa ilo kachiwiri.”

¹³⁵ Iye anali Mwamuna yekha yemwe akanakhoza kunena izo, yemwe anayamba wakhala wokhoza kunena izo, kapena yemwe adzayambe wakhlapo kuti anene izo. “Ine ndiri nayo mphamvu kuti ndiligoneke thupi Langa pansu; Ine ndiri nayo mphamvu kuti ndilidzutsa ilo kachiwiri.” Ndiko kulondola, Emanuele, Mwiniwake!

¹³⁶ Ndiyeno pamene Iye anafa, ndipo, pa tsiku la imfa Yake, iwo anamuchotsa Iye namusitsa pa mtanda, ndipo iwo anakamuika Iye mmanda. Ndipo Iye anagona mmenemo kuyambira Lachisanu madzulo mpaka Lamlungu mmawa, pa mmawa wodabwitsa uja wa Isitara pamene Iye anawuka kachiwiri. Ndipo moyo Wake unamasulidwa kuchokera ku ndende za gehena mmusi kutaliko, kumene Iye anapita ngati wochimwa mwa inu ndi ine, atanyamulira kutali machimo athu, kuti atipatse ife chitsimikizo changwiro. Palibe chifukwa chokaikira, panonso; kupereka chitsimikizo changwiro icho. Iye anati, “Ine . . .”

¹³⁷ Chifukwa Iye anachita izo, moyo Wake unaponyeredwa mu gehena, chifukwa Iye anali chotaidwa. Iye anali “azazeli” wa Chipangano Chakale,” yemwe, iwo ankaika machimo a anthu pa azazeli ndi kukaimasulira iyo ku chipululu kuti ikafe. Yesu anali azazeli ameneyo yemwe anali ndi machimo a anthu pa Iye, ndipo anakataidwa ndipo anapita ku gehena, kuti akawawidwe kuzunzidwa. Thupi Lake linapita mmanda, kuti alipire mtengo wa chiwukitsiro chathu. O, mai!

¹³⁸ Ndiye, pa mmawa wa Isitara uja, pamene Iye anabwerera kuchokera mmanda, kumene ululu wa imfa ndi gehena sizikanakhoza kumugwira Iye. Ndipo pamene Iye anawuka kachiwiri pa mmawa wa Isitara, osati kokha kuti Iye anawuka, koma pomweponso anabwera Yobu, Yakobo, Abrahamu, Isaki. Ena onse a iwo anabwera mu chiwukitsiro, mu Mateyu 27, “Ndipo anawonekera kwa ochuluka, ndipo konsekonse mmisewu.” Iwo a chisindikizo cha umboni wawo, chifukwa iwo anali ndi chinachake mwa iwo, chimene chinati, “Ine ndikudziwa Muomboli wanga alimoyo.” Ndipo kwa munthu aliyense . . . Tsopano, iwo ankadziwa!

¹³⁹ Mulungu ankadziwa, kuti mu masiku akudza, kuti azamulungu adzalizgwire Baibulo ili. Iwo ankadziwa kuti amuna anzeru akanadzalizgwire Ilo, kuti iwo akanadzaika kutanthauzira kwawo kwawo kwa Ilo, kuti iwo akanadzati, “O, Ilo silikutanthauza *izi*. Ilo silikutanthauza *izo*.”

¹⁴⁰ Chotero, kuti apange izo motsimikiza, kuti madongosolo Ake aakulu mu mibadwo yakudza akanati adzakwaniritsidwe . . . Mvetserani mwacheru tsopano pamene ife tikutseka msonkhano. Monga mu mibadwo yakudza, kuti dongosolo Lake likanati lidzakwaniritsidwe, Mulungu anapereka umboni wotsimikiza kwa izo.

¹⁴¹ Ife tikhoza kuwerenga Izo ndi kuti, “Ine ndikuzikhulupirira Izo.” Izo ndi mwamalingaliro. Icho ndi chikhulupiro chaluntha. Ndizo zamulungu zamwamalingaliro. Koma pali Chinachake chopitirira izo. Ndiko kulondola.

¹⁴² Osati kokha kuti Iye anawuka kuchokera kumanda, koma Iye anakwera Mmwamba ndipo anatomiza mmbuyo Mzimu

Woyera. “Iye anapita Mmwamba, ndipo anakapereka mphatso kwa anthu; anatsogolera amumsinga ku usinga, ndipo anapereka mphatso kwa anthu.”

143 Ndipo, lero, atatha azamulungu kusewera ndi Baibulo, utatha kukhazikitsidwa mpingo wa mabungwe, ndipo iwo akumati, “Chabwino, *izi* ndi zimene ife tikuzifuna. Anthu ena ataikidwa pansu pa tchalitchicho, ena a oyera; ife tikafukula ena a mafupa awo ndi kuwabweretsa iwo kuno.” Ena a iwo anati, “Ife timanga tchalitchi pa manda pamene Iye—pamene Iye anapachikidwapo, kapena pamene Iye anaikidwa. Ife timanga mpingo pamene.” Anthu, mu zogwirika, akuyesera kuti apange zinthu zogwirika, koma ndi zonyansa chomwecho. Palibe kanthu kwa izo. Zonse ndi zamkhutu, ndipo palibe kanthu kwa izo.

144 Koma chiwukitsiro chenicheni ndi iwo amene anafa ndi Iye, atabadwa kachiwiri, amene ali nacho chikhulupiriro “ndikudziwa chomwecho” chija. “Ine ndikudziwa Muomboli wanga alimoyo.” Ndipo Mulungu akugwira ntchito ndi anthu amenewo, “ndi zizindikiro ndi zodabwitsa,” ndipo kutumidwa kwakukulu pano, kukusonyeza kuti Iye anawuka kwa akufa, ndipo akusonyeza zizindikiro zowoneka ndi zodabwitsa.

145 Mulungu akudalitseni inu. Kodi inu mukuzikhulupirira izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi inu mukukhulupirira izo ndi mtima wanu wonse?

146 Ife titafulumirira kunyumba tsopano. Mukadye kadzutsa wanu ndipo mukabwererensu kachiwiri pa naini koloko. Ndipo ife tikuti tiwatumize anyamata kuno, kupereka makadi apemphero, pa naini koloko.

147 Ndipo kwa anga . . . ndikuti, mmawa uno, ndi mawu otsiriza pa izi pano, mpaka ine ndidzabwerere. Ambuye Yesu yemwe amene anawuka kwa akufa ali wamoyo lero, ndipo akhoza kuchita zinthu zomwezo monga Iye analonjezera. “Zizindikiro izi zidzatsatana nawo iwo amene akhulupirira, ngakhale mpaka ine ndidzabwerere kachiwiri.” Ngakhale inu mukhale mutatayidwa kunjira, ngakhale inu mukhale mukutchedwa “otentheka,” komabe Iye ali pano mwa Mphamvu Yake yonse. Mulungu akudalitseni inu. Ine ndikupemphera kuti Mulungu akupatseni inu Isitara, lero, kuti inu musadzaiwale konse utali wonse pamene inu muli moyo.

148 Tsopano, inu mukuti, “Kodi inu mukutsutsana nawo, anthu awo amene akupita ku mipingo, ndi mitanda yaikulu, ndi choncho?” Ayi, bwana, m’balé wanga. Zinthu zimenezo, zabwino monga izo zingakhale ziri, izo zangokhala monga kutenga . . . Pano pali chimene ine ndikuganiza za mipingo yaikulu imeneyo.

149 Inu mukuti, “O, zedi, ngati Ambuye akanatipatsa ife malo aakulu, ine ndikanayamikira izo.”

150 Koma pano pali kugamula kwanga kwa izo. Kodi inu munayamba mwaganizapo zopita kumusi kuno ku zipala ndi mafakitare, ndipo akumanga, sitima yaikulu, yaitali yonyamula anthu, yamakono, ndi mipando yonse yokongola, yopukutidwa, ndi wenzulo yaikulu pamwamba pake, ndi kuwaika oyendetsa mkati umo, popanda mpweya uliwonse kuti uziikoka iyo? Mukuona? Inu basi. . . Izo sizikanati zichite ubwino wa pang'ono. Ine kunalibwino ine ndikhale ndi galimoto yopukusa ndi dzanja kwinakwake, ili ndi mpweya mwa iyo, kuposa kukhala ndi zonse izo, (sichoncho inu?), chifukwa iwe upita nayo kwinakwake. Ndizo zoono. Chotero tsopano ingokumbukirani mophweka kuti, chiwukitsiro chenicheni, chinthu chenicheni.

151 Inu mukuti, “Chinthu chimenecho chikhoza kuyenda pachoka, kutali uko.” Ichu chingakhoze kuyenda bwanji? Mutsimikizire izo kwa ine.

152 Ndipo ndizo zimene ife tachita. Ife takonza mipando. Ife tapukuta wenzulo. Ife tawapukuta masikolala, kuti aziphunzitsa ndi zamulungu zazikulu, ndi kumagwiritsa ntchito mawu aakulu akulu amene angati basi. . . zinthu zazikulu zimene iwo amaziphunzira mu dikishonare, usiku wonse, kwa ulaliki, pafupifupi, kuti adzafike podzazitulutsa izo mmawa wotsatira, “mawu aakulu ofufuma.” Koma, m'bale, kwa ine, zimenezo ndi zamkhutu.

153 Ndipatseni ine Khristu. Ndipatseni ine chiwukitsiro. Ndipatseni ine umboni, mu mtima wanga, kuti Khristu anawuka kwa akufa. [M'bale Branham akugogoda pa guwa katatu—Mkonzi.] Izo zikhazikitsa icho, kwa ine. Amen.

154 Ndipatseni ine chinachake chimene ine ndingakhoze kunena, ndi Paulo wakale. . . Ndi chipinda chachikulu icho, chandima chiri pamenepo patsogolo pa ine, monga wachivundi. Ndipo ine sindine khanda panonso, kuti ine ndikudziwa nthawi iliyonse imene mtima wanga ugunda, ine ndikupita cha ku chipinda chachikulu chimenecho, chandima uko chotchedwa imfa. Nthawi iliyonse; ndipo tsiku lina iwo udzatenga kugunda kwake kotsiriza, ndipo ine ndiyenera kuti ndidzakalowe mchipinda chimenecho cha imfa ndi wachivundi aliyense.

155 Koma ine ndikufuna ndidzanene, ndi Paulo mtumwi wamkulu uja, pamene iye anati. “Ine ndikufuna kumudziwa Iye mu Mphamvu ya chiwukitsiro Chake,” kuti pamene Iye aitana kuchokera pakati pa akufa, ine ndidzatulukamo ndi Iye pa nthawi imeneyo.” Ndicho chimene ine ndikufuna, “kumudziwa Iye,” mmawa uno. Ndicho chimene, ine ndiri wothokoza kwa Mulungu, “Ine ndikumudziwa Iye mu Mphamvu ya chiwukitsiro Chake.” Kutu, “ine ndikudziwa Muomboli wanga alimoyo.”

156 Maso akhungu awa, amene nthawiyina anali akhungu, atsegulidwa. Thupi laling'ono ili, lokalamba lofooka, la pafupi

mapaundi zana ndi makumi awiri ndi asanu, likuzandima pano, lakhala liri . . . mnofu wabwera pa ilo. Mtima uwu umene nthawiyina unali wakuda ndi tchimo iwo wapangidwa kuyera. Zikhumbo izi zimene zinkakonda zinthu za mdziko, izo zinafa, zaka makumi awiri zapitazo, ndipo ilo lawuka kachiwiri tsopano.

¹⁵⁷ Ndipo maso achivundi awa amene ine ndimayang'ana kupyoleramo, ine ndakhala nawo mwayi, mwa chisomo cha Mulungu, kuti ndiziwawona olumala akuyenda, akhungu akuwona, o, zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa, ndi mphamvu za Mulungu. Ine ndikudziwa Muomboli wanga alimoyo. Ine ndikudziwa izo, kupyola mthunzi wa kukaika. Ine ndikudziwa izo. Ine ndikudziwa izo. Ine ndikudziwa izo Muomboli wanga alimoyo, ameni, mopitirira, nthawi zonse. Ngakhale imsyo zanga zitadyeka mkati mwa ine, ngakhale lirime langa litakanirira ku milomo yanga, ngakhale mphutsi za khungu zitalidya thupi langa, ngakhale atandimangira mwala pa manda, komabe, ine ndikudziwa Muomboli wanga alimoyo. Ameni.

Tingapemphere ife!

¹⁵⁸ Atate Akumwamba, ife tikukuthokozani Inu, mmawa uno, chifukwa cha chiwukitsiro ichi. O Mulungu! Poyamba, wochimwa, womangidwa ndi zingwe za tchimo; poyamba mu ndende, ndi zochitika; zamalubwelubwe, mwa chipukupuku, kuwopa imfa, kuwopa kukomana ndi Inu, koma tsiku lina laulemerero pamenepo panabwera chiwukitsiro kuchokera apo. Khristu anawuka mu mtima, ndipo lero ife tiri nacho chitsimikizo chachikulu ichi. Lero Iye alimoyo mwapamwamba, ndipo ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha Iye.

¹⁵⁹ Ndipo ife tikupemphera, Atate, tsopano, kuti Inu muwadalitse omvetsera apang'ono awa, ndipo ife tasonkhana. Mulole Mzimu Woyera Wanu upumule pa mmodzi aliyense. Inu mukhale ndi ife kupyola mu msonkhano ukudzawu, Ambuye. Ndipo mulole Mzimu Woyera ubwere pakati pathu mmawa uno ndi kudzachiza munthu wodwala aliyense yemwe ali mnyumba muno. Perekani izi, Ambuye. Mulole anthu azipita kuchokera pano, kuti azikakumbukira Isitara iyi kwa nthawi zonse. Perekani izi, Ambuye. Ndipo mulole zimphamvu zazikulu, mulole Angelo aakulu, amene anagudubuzana nachotsa mwala pa mmawa wa Isitara, mulole iwo ayime alipo, lero, kuti adzagudubuze mwala uliwonse wa kukaikira, mantha aliwonse, kusagwirizana kulikonse. Muzichotse izo ku mitima ya anthu. Perekani izi, Ambuye, kuti Mzimu Woyera ukhoze kubwera pansu mwa mphamvu yayikulu, ndipo ukhale ndi kufikira kwa aliyense. Perekani izi. Kupyolera mu Dzina la Yesu Khristu, ife tikupempha izi. Ameni.

¹⁶⁰ Tiyeni tiyime.

Woyamba kufera za Mzimu Woyera'wu,
Anali Yohane Mbatizi, koma anafa
mwaumunthu;
Ndiye anadza Ambuye Yesu, anampachika Iye,
Analalikira kuti Mzimu udzapulumutsa anthu
ku tchimo.

Ukuwukhabe magazi, inde, ukuwukha magazi,
Uthenga wa Mzimu Woyera ukuwukha magazi,
Magazi a ophunzira anafera Choonadi,
Uthenga wa Mzimu Woyera ukuwukha magazi.

O, anamugendapo Stefano, anatsutsa tchimo,
Anawakwiyitsa iwo, anamuphwanya mutu;
Koma anafa mu Mzimu, anapereka mzimu,
Nakalumikizana ndi, khamu lopereka-moyo.

Kunali Petro ndi Paulo, ndi Yohane
waumulungu,
Anapereka miyoyo kuti Uthenga uziwala;
Anasakaniza magazi awo, monga aneneri
akale,
Kuti Mawu a Mulungu awuzidwe moon.

Miyoyo pansu pa guwa, ikulira, “Mpaka liti?”
Kuti Ambuye alange anachita zolakwa;
Koma kukhala ena apereke magazi awo
Uthenga wa Mzimu Woyera ndi mtsinje
wofiira.

Ukuwukhabe magazi,
Uthenga wa Mzimu Woyera ukuwukha magazi,
Magazi a ophunzira anafera Choonadi,
Uthenga wa Mzimu Woyera ukuwukha magazi.

¹⁶¹ Kodi inu simukumukonda Iye? Ife timaimba nyimbo yaying'ono imeneyo chifukwa ife tikukhulupirira kuti Uthenga wa Mzimu Woyera ukadawukha ndi Magazi. Ndiyo njira ya kuzunzidwa. Ndiyo njira ya kusamvetsedwa. Ndiko kulondola. Dziko silikuwudziwa Iwo. Dziko silimaudziwa nkomwe Iwo. “Dziko lidzakudani inu. Koma mukhale a chisangalalo chabwino, Ine ndaligonjetsa dziko.” Iwo samaumvetsa Iwo. “Kulalikira kwa mtanda ndi zopusa kwa iwo amene akuwonongeka.” Koma pali Chinachake pansu mu mtima wa wokhulupirira, amati, “Ine ndikudziwa Muomboli wanga alimoyo. Ine ndikudziwa izo, kupyola kukaikira.”

¹⁶² Aliyense akumverera bwino? Ati, “Ameni.” [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Tsopano gwiranani chanza ndi wina amene waima pafupi ndi inu, muti, “Ambuye alemekezeke.” Ambuye alemekezeke. Ambuye alemekezeke. Ambuye alemekezeke. Ndizo zabwino. Ndizo zabwino.

¹⁶³ Tengani malo anu, mmawa uno, ndi Khristu. Iye anawuka kwa akufa. Tengani njira ndi onyozedwa apang'ono a Ambuye. Chabwino.

Tsopano tingaweramtse mitu yathu mphindi yokha.

¹⁶⁴ Ndipo tsopano kumbukirani mautumiki mu maminiti pang'ono okha kachiwiri. Ife tiyamba kachiwiri, tsopano, pa—pa naini koloko; makadi apemphero adzaperekedwa. Teni koloko, Ambuye akalola, akalambulabwalo adzayamba. Utumiki wa kulalikirira udzayambika pofika pafupi iyo, pafupi—pafupi teni, ine ndikuganiza. Ndipo inu mudzakhale pano molawirira, pa naini koloko, kuti mudzatenge makadi anu a pemphero. Ndipo anyamata adzakhala ali pano akupereka makadi a pemphero pa naini koloko, mmawa uno. Chabwino.

¹⁶⁵ Tsopano fulumirirani kunyumba. Ngati inu muyenera kuti mukadye, pitirirani. Ngati simukatero, mukabwerere opanda kadzutsa. Mai, ife timadya mochuluka kwambiri, mulimonse. Chotero ndiye mukabwerere, mukusala, mukusangalala, lolani mtima wanu ukhale mwabwino.

¹⁶⁶ Mungozisunga izo mu malingaliro anu, “Ine ndikudziwa Muomboli wanga alimoyo. Ine ndikudziwa Iye ali. Mabelo achisangalala akuimba mu mtima wanga! Chifukwa Iye anawuka, ine ndidzawuka nawonso. Pakuti, ine ndiri kale, moyembekezera, mwapamalo wowukitsidwa limodzi ndi Iye tsopano, ‘ndikukhala mu malo a Mmwambamwamba mwa Khristu Yesu.’”

¹⁶⁷ Tsopano tiyeni tiweramtse mitu yathu, paliponse mu chipinda. Ndipo ine ndamufunsa M'bale Beeler, mmodzi wa azibusa pano . . .

¹⁶⁸ M'bale Tom Meredith, ine ndinamuwona iye kumbuyo uko, aponso, ife timugwiritsa iye ntchito mu utumiki kanthawi kenako.

¹⁶⁹ Ndipo tsopano M'bale Beeler, ngati iye angaponde patsogolo pamene aliyense ali ndi mutu woweramitsidwa mu pemphero, ife timupempha iye kuti atibalalitse ife mwa pemphero. Chabwino, M'bale Beeler, ngati inu mungatero.



MUOMBOLI WANGA ALIMYO CHA55-0410s
(My Redeemer Liveth)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikidwa mu Chingelezi pa Lamlungu la Isitara mmawa pa kutuluka kwa dzuwa, Epulo 10, 1955, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mchaka cha 2000 ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2000 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org